**EXAMINATIONS COUNCIL OF ZAMBIA**

**Examination for General Certificate of Education Ordinary Level**

# Cinyanja **3156/2**

**Paper 2**

**Wednesday** **20 JULY 2016**

Additional materials
Answer Booklet

**Time 2 hours**

## Instructions to candidates

Write your name, centre number and candidate number in the spaces provided on the Answer Booklet.

www.eczpastpapers.com

You should refer to the instructions printed overleaf with the questions.

Write your answers in the separate Answer Booklet provided.

If you use more than one Answer Booklet, fasten the booklets together.

## Information for candidates

The number of marks is given in brackets [ ] at the end of each question or part question.

**Cell phones are not allowed in the examination room.**

**Nthawi:** Maola awiri

## Malangizo kwa olemba mayeso

Lemba dzina lako, nambala ya malo kumene ulembera mayeso ndiponso nambala yako iwe amene ulemba mayeso. Ulembe izi m'malo omwe apatsidwa m'kabuku ka la mayankho.

Uziwerenga mobwereza-bwereza ndi kumvetsetsa malangizo omwe alembedwa pamwambapa ndi mafunso.

Lemba mayankho ako m'kabuku ka mayankho komwe kapatsidwa. Ngati wagwiritsa nchito mopitirira kabuku kamodzi, umange pamodzi mwatsatane-tsatane timabuku tonse wagwiritsa nchito.

## Zina zolangiza olemba

Nambala ya mamaliki yaikidwa mu mfungato [ ] kumatsiriziro a funso liri lonse kapena kumbali ya funso kapena kumphepete kwa funso mwatsatanetsatane.

©ECZ/2016/GCE/F1

**This question paper consists of 6 printed pages.**

www.eczpastpapers.com

## CIGAWO COYAMBA – KUMASULIRA [20]

Yankhani mafunso onse mcigawo ici.

1 **Tembenuzani M'cinyanja cabwino nkhani iri munsimu.**

### THE END OF SLAVERY

The captives knelt down in their way of expressing thanks, clapped their hands with great energy. They were thus left entirely in our hands and knives were soon busy at work, cutting loose the women and children. It was more difficult to free the men, as each had his neck in the fork of a stick and kept in by an iron rod which was riveted at both ends across the throat. With a saw luckily in the Bishop's baggage one by one the men were sawn out into freedom. The women on being told to take the meal they were carrying and cooked breakfast for themselves, men, women and children seemed to consider the news too good to be true.

## CIGAWO CACIWIRI – MVETSO [30]

2 **Weregani nkhani iri munsimu ndipo bwino lake muyankhe mafunso otsatira nkhani.**

**NKHANI**

**Tsopano panali patapita mwenzi umodzi kucokera pamene anatentha chire la Manondo.**

Kacipande anamemeza cisokole. M'mawa mwake anthu anasonkhananso m'mudzi wa a Njoka. Atasonkhana anthuwa anayamba adyera. Pambuyo pake cisokole cinakwera Phiri la Nyaze, ndipo unali mpambu waukulu wa anthu. M'phiri muja Msandinyoze www.eczpastpapers.com anapha cinkhoma, pamwamba pa Phiri anabvundumutsa ngoma, ndipo mpoto wina pothawira Msongwe, unadzera kumene kunali Msatero ndipo iye anaulasa ndi ncheto nati "Wakwata bano!" Mpoto uja nufa pomwepo. Kacipande anapha nguluwe ya ana. Cimwendo anacita mwainayenso tsikulo, ndipo anapha kasenye.

Alikusaka tero, Kapsyala anapeza mwana wa insa pambuto, nammenya ndi nkholi ndi kufera pambuto pomwepo. Mwiri poti adzere kwa ciphwafu, anakuma ndi cimtunga nafa pomwepo. Koma Mapundu pamene anafuna kulasa imodzi mwa nguluwe zija za mphongo anaphonya, mubvi wake nulasa ku mtengo pakuti anatengera mabvubvu. Ngakhale nguluweyo anaikhuwizyira agalu, inagodoboka Phiri osaipezanso.

Ena ocokera kumidzi yina anapha nyama zao zosiyana-siyana koma pambuyo pake galu wa Mapundu Zatonse anagwira Sakwimbala.

Tsono pamene cisokole cinatsikira kuseri kwa phirilo pofika m'dambo Zunguze anapha cozimbi ndipo nyamayo anagawirako Mapundu ndi Ciphwafu.

Koma anthu amene anapha nkhanga ndi nkhwali anali osawerengeka, cifukwa ngakhale zinali kuuluka ndi kukagwa kutali cifukwa coculuka kwa anthu anali kuzipezanso. Zamwai zinali zimene zinali kumaulukira kumbuyo kwa cisokole, koma zonse zoulukira kumpandu, zinafikira ku nkholi pena kugwidwa ndi agalu zikalema.

Ataoloka dambolo, pofika kumtunda nkhwali yina inalowa pa cipata ndipo cimwendo anaitsatira pamenepo koma potulukapo, citedze cinamuyabwa ndipo anayamba kudzikandula thupi lonse. Ndipo Mapundu anati, "Kodi watani Cimwendo?"



www.eczpastpapers.com

Cimwendo anamuuza Mapundu kuti anayabwidwa ndi citedze. Panapita nthawi yaitali kuti kunyerekesa kwa citedze kuja kuleke.

Popita patsogolo, Ciphwafu analumidwa ndi mabvu amene anali mumtengo wa bwazi. Umene unali pafupi ndi matowo amene iye anali kuthyola kuti andye.

"Uthyolerepo kasanthi kuti ululu ucoke onse msanga," anatero Kapsyala kuuza Ciphwafu. Ciphwafu anacita monga momwe anamuuzira koma popeza sanali mabvunkhomola, Mabvuwo, Ciphwafu sanabvutike kweni-kweni pofika madzulo Cisokole cija cinatha bwino lomwe panalibe zobvuta zina.

Pakutha kwa cisokole, aliyense amene anapha nyama anapereka mwendo wathako kwa Kacipande monga mwalamulo.

Anthu a m'mudzi wa a Njoka anapezanso nyama tsiku lija. Koma iwo amene anapha misulu, nkhanga, nkhwali, a mwiri, mbira ndi a sakwi zonse anali kutenga osapatsako mwini cisokole popeza lamulo lake linali tero.

**Mafunso**

**Tsopano yankhani mafunso otsalira awa.**

1 Kucokera m'ndime yoyamba nyama zinaphedwa zinali ...

- **A** imodzi.
- **B** ziwiri.
- **C** zitatu.
- **D** zinai. [1]

www.eczpastpapers.com

2 Ndime ya ciwiri itifotokozera kuti nyama imene inathawa ndi ...

- **A** Nguluwe.
- **B** Mwiri.
- **C** Insa.
- **D** Cimtunga. [1]

3 M'ndime ya cinai muli mau awa akuti, "Zamwai zinali zimene zinali kuulukira kumbuyo kwa cisokole," apa atanthauza ...

- **A** Nyama.
- **B** Nkhanga.
- **C** Nkhwali.
- **D** Nkhanga ndi nkhwali. [1]

4 M'ndime ya cisanu, anayabwidwa anali ...

- **A** Cipeta.
- **B** Cimwendo.
- **C** Mapundu.
- **D** Ciphwafu. [1]



www.eczpastpapers.com

5 Ciphwafu analumidwa ndi mabvu cifukwa ca ...

A matowo.

B bwazi.

C nyama.

D kapsyala. [1]

**Yankhani mafunso otsatira awa polemba ziganizo zathunthu.**

6 Fotokozani malamulo amene analiko ku cisokole ngati munthu wapha nyama. [4]

7 Ndi zotani zimene anthu aja anali kugwiritsa nchito pakupha nyama ku cisokole. [4]

8 Nkhanga zoulukira kumpandu zinali kupeza imfa bwanji? [3]

9 Lembani mau amene ali ndi matanthauzo olingana ndi awa amene ali m'nkhani mwawerengayi.

(i) Nkhalango (mu ndime 1) [1]

(ii) Camutunga (mu ndime 2) [1]

(iii) Kumtsiriziro (mu ndime 4) [1]

(iv) Kudzikandula (mu ndime 5) [1]

(v) Kankhuni (mu ndime 8) [1]

www.eczpastpapers.com

(vi) Zengero (mu ndime 8) [1]

(vii) Udzu utali-utali (mu ndime 5) [1]

(viii) Mwendo wa mbuyo (mu ndime 9) [1]

10 **Tsopano perekani matanthauzo a mau awa:-**

(i) Pa mbuto [1]

(ii) Mabvubvu [1]

(iii) Godoboka [1]

(iv) Ululu [1]

(v) Wakwata bano [1]

(vi) Mpambu [1]



www.eczpastpapers.com

## CIGAWO CACITATU - CINENEDWE [30]

3 *Yankhani mafunso* **onse asanu**

(a) Pangani mau ndi zindunswa za mau ziri munsimu ndipo pambuyo pake mupereke tanthauzo la cindunswalo

(i) –na [1]

(ii) –na– [1]

(iii) –ta– [1]

(iv) –ika [1]

(v) –nga– [1]

(vi) –ula– [1]

**[6]**

(b) M'munsimu muli ziganizo zimene inu muyenera kuzilembanso pambuyo pake mupeze apamneni alimo ndipo mulembe mzere munsi mwa pamneni amene mwapeza.

(i) Yohane aphunzira ku Chizongwe. [1]

(ii) Amalume anabwera caka catha. [1]

(iii) Kodi aphunzitsi a Zulu apita kuti? [1]

(iv) Akuti lagwa m'dzenje galimoto. [1]

(v) Mwana akudya mwaubve ndi wanu? [1]

www.eczpastpapers.com

(vi) Muziimba mokuwa kuti timve. [1]

(c) Pali aperekezi anai odziwika m'cinyanja

(i) Chula aperekeziwa. [2]

(ii) Gwiritsira nchito mperekezi aliyense wachula pa mwambapa m'ciganizo colongosoka. [4]

(d) Lemba matsinde ophatikizana kucokera ku maina awa:

| **Citsanzo: dzina** | **matsinde ophatikizana** |
|---|---|
| mtondo | msemamitondo |

(i) thabwa [1]

(ii) uci [1]

(iii) ng'amba [1]

(iv) njiru [1]

(v) tiki [1]

(vi) nkhanga [1]

(e) Ziganizo ziri m'munsimu ndi zolakwiika zilembeni m'cinyanja coyenera.

(i) Tipereka njinga atatituma. [1]

(ii) Amulembi sadalembe kalata ya msokhano dzulo. [1]

(iii) Anakabyala cimanga mofolumira anakakola cambiri. [1]



www.eczpastpapers.com

(iv) Ndidziwa abusa adwala cifukwa nthawi zonse sacedwa kuyambitsa mapemphero. [1]

(v) Yohane anapemphedwa kubvalako ku nyumba. [1]

(vi) Yege wapita kukaonerera mpira ku Kitwe. [1]

## CIGAWO CA CINAI – MIYAMBI NDI MIKULUWIKO [20]

Mukakamisizdwa kuyankha miyambi isanu cabe kucokera kufunso 4A ndi mikuluwiko isanunso kucokera la 4B.

4 (a) **MIKULUWIKO**

Perekani matanthauzo a **Mikuluwiko** isanu cabe mwa khumi iyi munsimu. Mukatero mupange **ziganizo** ndi **mikuluwikoyo** kuonetsa kuti mukuidziwadi.

**Citsanzo:** mkuluwiko = Dovu

Tanthauzo = Nkhuli

Ciganizo = Yosefe ali ndi dovu

(i) Fudya [2]

(ii) Chipere [2]

(iii) Bwize [2]

www.eczpastpapers.com

(iv) Dendedza [2]

(v) Chiphapha [2]

(vi) Sathaphazi [2]

(vii) Kusamira dzanja [2]

(viii) Dwala [2]

(b) **MIYAMBI**

Perekani matanthauzo a **miyambi** isanu cabe mwa iyi:

(i) Kucenjeza camphongo. [2]

(ii) Ukapeza anzako akazinga maso, nawenso tong'ola ako. [2]

(iii) Tikonze tikonze adanyula maliro ya eni. [2]

(iv) Kwa eni kulibe mkuwe. [2]

(v) Cizolowezi ca namkholowa cidaulultsa mbatata. [2]

(vi) Madzi saiwala khawa. [2]

(vii) Kumanga khobwe ndi m'mawa. [2]

(viii) Pakadafunda padajiwitsa galu. [2]

**KWATHA**

www.eczpastpapers.com